22100055

International Baccalaureate®
Baccalauréat International
Bachillerato Internacional

**CHICHEWA A1 – STANDARD LEVEL – PAPER 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEAU MOYEN – ÉPREUVE 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEL MEDIO – PRUEBA 1**

Thursday 13 May 2010 (afternoon)
Jeudi 13 mai 2010 (après-midi)
Jueves 13 de mayo de 2010 (tarde)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

INSTRUCTIONS TO CANDIDATES

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a commentary on one passage only. It is not compulsory for you to respond directly to the guiding questions provided. However, you may use them if you wish.

INSTRUCTIONS DESTINÉES AUX CANDIDATS

- N'ouvrez pas cette épreuve avant d'y être autorisé(e).
- Rédigez un commentaire sur un seul des passages. Le commentaire ne doit pas nécessairement répondre aux questions d'orientation fournies. Vous pouvez toutefois les utiliser si vous le désirez.

INSTRUCCIONES PARA LOS ALUMNOS

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un comentario sobre un solo fragmento. No es obligatorio responder directamente a las preguntas que se ofrecen a modo de guía. Sin embargo, puede usarlas si lo desea.





© International Baccalaureate Organization 2010

https://xtremepape.rs/

*Lembani ndemanga pa nkhani* ***imodzi*** *mwa nkhani ziwiri zili m'munsizi. Simukuwumirizidwa kuyankha mafunso okutsogolerani amene alembedwa m'munsimu. Komabe ngati mukufuna kutero mungathe kuwagwiritsa ntchito.*

**1.**

Tsiku lina, Lamulungu, tidatengana ndi Enifa kupita ku msika. Tikuyenda mumsikamo, tidafika pamalo pogulitsira nsomba zaziwisi. Mkulu wina adandipatsa moni kenaka nkudzampatsa mkazi wanga moni amvekere: "Moni apongozi."

Titachoka pamalopo, ndidamufunsa, "Tandiuza Enifa. Kodi mkulu uja amati, moni apongozi, ndi yani? Ndipo chipongozi chake chachokera kuti?" Enifa adaseka. "Ukuseka? Ndikuti ndiyani?"

"Inenso sindikuwadziwa. Mwina chifukwa chondionaona mumsika muno."

"Siyankho lokwanira limenelo. Iwe kuno kumsika umabwera kangati? Kodi mumsika uno umapezeka mkazi iwe wekha?" Enifa adasekanso.

Kusekaku kudapitirira kundipsetsa mtima. Sindidasamalenso zoti tinali mu msika.

"Cheteka, hule!" Enifa adasiya kusekako. Adaonetsa nkhope yokhumudwa.

"Kanthumbo, mpaka kundinena kuti hule? Ngati ndili hule, udandikwatira chifukwa chiyani? Kodi akazi ena amene sali mahule, sudawaone nkale lonse?"

Tidatuluka mumsikamo osalankhulananso mpaka tidakafika kunyumba. Kucha kwa tsiku Lolemba, ndididzuka kupita kubafa. Amene adandikonzera mtenthandevu adali mtsikana wantchito. Enifa adali gone pa bedi. Adakwiyiratu. Nditatha kumwa mtenthandevu ndidamulawira Enifa, koma iye sadayankhe. Ndidatuluka kukakwera galimoto kumapita kuntchito.

Zomwe Enifa, mkazi wanga, adachita tsiku limeneli ndidazunzika moyo wanga. Enifa adandiyimbira telefoni yondiuza kuti kunyumba kwanga wachokako. Ndidamuona akukwera basi yopita ku Zomba, ndidaona ngati moyo wanga ukufuna kutuluka m'chifuwa mwanga. Ndidakwera basi yopita ku Ndirande komwe ndinkakhala naye m'chinyumba chathu chachikulu, kuti ndikaone Annie, Nita ndi Nenani. Nditatsika basi ku Ndirandeko ndidayenda mofulumira kupita kunyumba. Nditalowa, Annie ndi abale ake aja sadadziwe kuti ndafika. Nthawi imeneyi ndidapeza ana angawo akukanganirana phala la mu poto. Ndidamva chisoni chachikulu pamene ndidamuona Nenani akuthamangira pambuyo kuti mwina akadapezako kangachepe kuchokera m'poto muja.

"Annie," ndidaitana, nkumugwira mkono mwachikondi.

"Bambo," adavomera nagwetsa nkhope chifukwa cha manyazi.

"Kodi mayi anu apita kuti?" Ndidafunsa.

"Sindikudziwa" adayankha Annie nkhope yake ikuyang'anabe pansi.

"Sadakuuzeni kumene apita panthawi imene amachoka?"

"Ayi. Sadatiuze. Sadatilawirenso. Nthawi yomwe mayi amatuluka pakhomopa nkuti atanyamula katundu wina. Nenani adalira kuti apitire limodzi, koma iwo anangoti sachedwa, akupita kuchipatala kukabayitsa jekeseni," adafotokoza Annie ngati munthu wamkulu.

Misozi idatuluka. Ndidaponya maso pamwamba pa kabati. Ndidaona kapepala katatsamiridwa ndi chipeso. Ndidanyamula kapepalako. Panalembedwapo mawu pang'ono.

"*... Ndaona kuti iwe Kanthumbo, sudzandikhulupiriranso monga mkazi wako. Ndapita mbali ya Zomba kukakhala ndi amene aja udandipeza nawo aja, amene aja unkati sadayenera kukhala apongozi anga. Ndaona kuti zoonadi zenizeni tsopano zichitike. Ndimakana mwamuna kundizunguza mutu ngati dziko lonse lino mwamuna ndi mmodzi. Ndidangofuna kukhala nawe kwa nthawi yochepa kuti ndione kupusa kwako...*"



https://xtremepape.rs/

Ndidalephera kupitiriza kuwerenga chifukwa misozi idatsika m'maso mwanga, ndidakaponya pansi kapepalako. Ndidamulawira msungwana wantchito uja nkumulangiza kuti asamale ana aja n'kuwauza kuti ndibwera tsiku linalo. Nditafika ku Zomba ndidayenda m'sitolo, malo onse ogulitsira mowa, odyera, koma Enifa sindidamuone.

M'mawa wa tsiku linalo ndidapita kumsika. Ndidalowa mumsikamo, kwina ndikuponyaponya maso ngati ndikadaona nkhope ya Enifa. Ndidagula nthochi nkukhala pansi kuti ndiyambe kudya. Nditangosenda nthochi imodzi kuti ndidziika mkamwa ndidaona nkhope ina yofanana ndi Enifa atanyamula basiketi kudzanja ndipo pambalipa pali munthu wamwamuna nkhope yake ngati yomwe ya munthu wa kumsika ankati apongozi kunena mkazi wanga, Enifa. Sindidakhulupirire zomwe ndidaonazo.

Atatuluka panja ine ndinali pambuyo pawo. Nthawi imeneyi basiketi atanyamulizana mpaka adafika pamalo pamene padayima galimoto ya mtundu wa *Peugeot*. Mkulu uja ndi Enifa adalowa m'galimotolo nakhala mpando wakutsogolo. Sadatseke chitseko msanga. Enifa adawerama namupsopsona mkulu uja. Pamenepo, ndidamva kena kake ngati kakuyendayenda m'mutu mwanga. Ndidaona ngati ndidachita chizungulire. M'maso mwanga mudachita mdima. Sindidziwa momwe ndidayendera kuti ndikapezeke ndili pagalimotopo.

Nixon Mindano, *Chakondawini Mlekere*

– "Njovu zikamamenyana umavulala ndi udzu." Tsimikizani mawuwa malinga ndi zomwe zikuchitika munkhaniyi.

– Fotokozani luso limene mlembi wagwiritsira ntchito kuti owerenga athe kutsatira nkhaniyi mosavuta.

– Fotokozani momwe mlembi wagwiritsira ntchito malo amene akuchikitikira nkhaniyi ndi zotsatira zake pankhaniyi.



https://xtremepape.rs/

**2.**

**Misozi Ya Chumba**

Zitsime za misozi nzosaphwa m'masomu.
Nkhawa yazendewera moyo wanga.
Mtendere wandithawa ngati chithunzi mumdima.
Tulo sintidziwa
Maganizo oganga mutu nawo ngosandithera.

Ndavutika mnzanune.
Ndazunzika ine
Usiku ndi usana ndikhalira kufwenthera nkusisima.
Masowa ngachifiirireni ngati utchazo.
Komwe akuchita amunangaku sikumenya.

Mkati mwa usiku, anthu ali mkafe
Amatulukira ali dzandidzandi.
Koma akayamba kundiyoyolera mawu achinyozo
Ndimachita kukhala ngati ndayabwidwa n'chitedze.
Anzanga ndidalakwanji ine?

Mayina ondipatsa ngamayereyere.
Ena anditcha chumba mwinanso chimbwira
Anzawo nati ndine chidangoyera
Kundiseka chifukwa cha kuuma kwanga.
Abale sindidapemphe chilemachi.

Nsalautu yalekaleka nane ndimayifuna
Koti ndidzikatuma kumsika ndimakakhumba.
Nanga chondisekera kupunduka nchiyani?
Mwanditha nzeru anthu inu.
Mwandiumitsa thupi ndi nkhanza zanu.

Pondinyodola kumadzi,
Pondijeda kumtondo
Musamayiwale kuti nanenso ndine munthu.
Mukamandiseka kumphambano,
Nkumandilalatira ku gule,
Muzikumbuka kuti adandilenga choncho Chauta.

Benedicto Wokomaatani Malunga, *Kuimba Kwa Mlakatuli* (1990)

– Fotokozani momwe mlembi akugwiritsira ntchito mawu pofuna kuti ndakatuloyi ikhale yozama komanso yothyakuka bwino.

– Ndakatuloyi ikutiwunikira mavuto amene amadza kamba ka miyambo kapena zikhulupiriro zimene zimakhalapo pakati pa anthu. Perekani maganizo anu pamfundoyi.

– Fotokozani za amene akuyankhula mu ndakatuloyi ndi uthenga wome akupereka.



https://xtremepape.rs/